Kodi ndi chifukwa chiyani FISPs

ikulephela kukwaniritsa zolinga zake?

Ndondomeko ya zipangizo zaulimi zotsika mtengo (FISPs) mophatikizika mu machitidwe a ntchito za Green Revolution zalephela kufikila kuwonetsetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira, kutukula miyoyo ya anthu akumidzi, ndi kuchepetsa umphawi. **M'MALO MWAKE**, yalenga moyo wodandaulitsa wodalira mwa alimi pa zipangizo zimene zimapelekedwa (mbeu zovomelezeka, foteleza, ndi mankhwala ophela tizilombo) ndi kuwakakamizira mu msampha wa ngongole zosatha.

Ziphaso, foteleza ndi zipangizo zina kawirikawiri zimasowa kapena kubedwa zisanawafikire alimi. Alimi amene amalandi zimenezi kawirikawiri amazigulitsa kwa alimi ochita bwino.

Zina mwa njira zosankhira opundula nawo kuchokela ku ndondomeko ya FISP ndi magulu a anthu amene ali pa ziwopsyezo zosiyanasiyana – makamaka alimi achizimayi – amene amasalidwanso ndi athu ogwira ntchito ku boma komanso mafumu a m'mudzi.

Ndondomeko za FISP **sizimathandiza** mayiko kuti akhale wopilira komanso malimidwe okhazikika komanso ndondomeko za zakudya zokhazikika. M'malo mwake zimawonjezera njala komanso umphawi, komanso kuwonongake kwa nthaka ndi madzi a ku Africa.

dudu coelho.com

african centre for biodiversity

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156